



# العَقِيدَةُ لِلأَطْفَالِ

**‘Aqīdah kwa Ana**

**Mlembi:**

Abū Hashmah Al-Malāwī

**Editor:** Uthmān Chikapa

**Buku 3**

## ZA MKATIMU

TANTHAUZO LA TAWHĪD .....	3
MITUNDU YA TAWHĪD.....	6
CHOTSUTSANA NDI TAWHĪD.....	9
ZITSANZO ZA SHIRK.....	12

# مَعْنَى التَّوْحِيدِ

## TANTHAUZO LA TAWHĪD

At-Tawhīd (pa chiyankhulo) ikutanthauza: kuchipanga chinthu kukhala chimodzi. **التَّوْحِيدُ: هُوَ جَعْلُ الشَّيْءِ وَاحِدًا.**

Ndipo At-Tawhīd mu Chisilamu ikutanthauza: **وَالتَّوْحِيدُ فِي الإِسْلَامِ هُوَ:**

Kumupatula Allāh mu ntchito zonse za ‘ibādah. **إِفْرَادُ اللَّهِ بِالْعِبَادَةِ.**

Ndipo Tawhīd imeneyi, ndiyo tanthauzo la mawu ako oti: **وَهَذَا التَّوْحِيدُ هُوَ مَعْنَى قَوْلِكَ:**

Palibe wina wopembedzedwa koma Allāh. **لَا إِلَهَ إِلاَّ اللَّهُ.**

Ndipo liwu limeneli lili ndi nsanamira ziwiri: **وَلِهَذِهِ الْكَلِمَةِ رُكْنَانِ،**

Zomwe ndi Chiletso komanso Chitsindikizo. **فَهُمَا النِّفْيُ وَالْإِثْبَاتُ.**

Chiletso chomupangira Allāh Shirk ya mtundu ulionse, **نَفْيُ الشِّرْكِ لِلَّهِ مِنْ كُلِّ وَجْهِ،**

Komanso kuvomereza za Kumupembedza Allāh Yekha basi. **وَإِثْبَاتُ الأُلُوْهِيَّةِ لِلَّهِ وَحْدَهُ.**

Ndipo ndithudi kulondola kwa chikhulupiriro  
(chathu) mwa Allāh,

وَإِنَّ تَحْقِيقَ الْإِيمَانِ بِاللَّهِ،

Kwagona pa Kumupatula Allāh Yekha  
mu ‘ibādah.

يَكُونُ بِإِفْرَادِ اللَّهِ وَحْدَهُ بِالْعِبَادَةِ.

Choncho, amene watembenuza china  
chilichonse (kuchokera mu ‘ibādah) ndi  
kupangira wina posakhala Allāh,

فَمَنْ صَرَفَ شَيْئًا مِنْهَا لِغَيْرِ اللَّهِ،

Basi ameneyo ndi womuphatizikira Allāh  
Wapamwambamwambayo.

فَهُوَ مُشْرِكٌ بِهِ سُبْحَانَهُ.

تَمْرِين

NTCHITO

**1. Kodi Tawhīd ndi chiyani?**

Mwana adziwe tanthauzo lolondola la Tawhīd.

**2. Kodi Tawhīd mu chisilamu yakhazikika pa nsanamira zingati?**

Mwana azindikire kuti Tawhīd yatsamira pa nsanamira ziwiri: kutsutsa chilichonse chomwe chimapembedza posakhala Allāh, komanso kuvomereza zoti wopembedzedwa mwa choonadi ndi Allāh Yekha basi.

**3. Kodi kupanga du’ā kwa wina posakhala Allāh ndi gawo la Tawhīd?**

Mwana aphunzitsidwe momveka bwino kuti du’ā ndi gawo la ntchito zomuchitira Allāh Yekha basi. Sizili zololedwa mu Chisilamu kuti munthu apange du’ā kwa Mtumiki wa Allāh (ﷺ), ‘Ali Ibn Abī Twalib, Al-Husayn Ibn ‘Ali, Al-Hasan Ibn ‘Ali, Fātwimah bint Muhammad, Ahmad Al-Badawī, ‘Abdul-Qādir Jaylān, Yesu ngakhalenso kwa mngelo aliyense.

**4. Kodi msilamu akhulupirire chani pa nkhani ya Tawhīd?**

Mwana athe kufotokoza kuti Tawhīd ndiye chipambano cha munthu pa dziko pano komanso ku Ākhirah.

**5. Kodi yemwe wamwalira asali pa Tawhīd adzakalowa kuti?**

Mwana adziwe kuti aliyense amene wamwalira asali pa Tawhīd ameneyo akalowa ku Moto ndipo akakhalako mpaka kalekale.

# أَقْسَامُ التَّوْحِيدِ

## MITUNDU YA TAWHĪD

اعْلَم، أَنَّ لِلتَّوْحِيدِ ثَلَاثَةَ أَقْسَامٍ: Zindikira, ndithu Tawhīd ili mu mitundu yokwanira itatu:

تَوْحِيدُ الرُّبُوبِيَّةِ، وَتَوْحِيدُ الْأُلُوهِيَّةِ، Tawhīd Ar-Rubūbiyyah, ndi Tawhīd Al-Ulūhiyyah...

وَتَوْحِيدُ الْأَسْمَاءِ وَالصِّفَاتِ. Komanso Tawhīd Al-Asmā' ndi As-Swifāt.

فَتَوْحِيدُ الرُّبُوبِيَّةِ مَعْنَاهُ... Tsopano Tawhīd Ar-Rubūbiyyah tanthauzo lake ndi:

تَوْحِيدُ اللَّهِ بِأَفْعَالِهِ. Umodzi wa Allāh mu ntchito Zake.

وَأَصُولُهَا: الْخَلْقُ وَالْمُلْكُ وَالتَّذْيِيرُ. Ndipo mapata ake a (Tawhīd iyi): Allāh ndiye Wolenga, Mwini, komanso Woyendetsa zinthu.

وَتَوْحِيدُ الْأُلُوهِيَّةِ أَوْ تَوْحِيدُ الْعِبَادَةِ: Ndipo Tawhīd Al-Ulūhiyyah kapena Tawhīd Al-'Ibādah:

إِفْرَادُهُ تَعَالَى بِالْعِبَادَةِ، Kumupatula Allāh mu ntchito za 'ibādah,

وَالتَّأَلُّهُ لَهُ، وَالخُضُوعُ وَالدُّلُّ. Komanso kudzipereka kwa Iyeyo, ndi kugonjera mwa Iye, komanso kudzichepetsa pamaso Pake.

Komanso kukhala ndi Chikondi chodzadza pa Iye,  
komanso kukhala wosaukira zomwe Iyeyo ali Nazo.

وَالْحُبِّ وَالْإِفْتِقَارِ،

Ndi kutembenukira kwa Iyeyo  
Wapamwambamwambayo

وَالْتَوَجُّهِ إِلَيْهِ تَعَالَى.

Ndipo Tawhīd Al-Asmā' ndi As-Swifāt:

وَتَوْحِيدُ الْأَسْمَاءِ وَالصِّفَاتِ:

Allāh ndi m' modzi mu Mayina Ake.

أَنَّ اللَّهَ وَاحِدٌ فِي أَسْمَائِهِ.

Ndi kumusimbanso Allāh Wapamwambamwamba

وَأَنَّ يُوصَفَ اللَّهُ تَعَالَى

Kudzera mu zomwe adadzisimbira nazo Iye Mwini,

بِمَا وَصَفَ بِهِ نَفْسَهُ،

Komanso ndi zomwe adamusimbira nazo Mtumiki  
Wake (ﷺ).

وَبِمَا وَصَفَهُ بِهِ نَبِيِّهِ ﷺ

Motsutsa ndi motsindika:

نَفِيًّا وَإِثْبَاتًا:

Choncho, zitsindikizidwe pa Iye (Allāh) zomwe  
Mwini Wakeyo adazitsindika (mu mbiri Zake),

فِيثْبَتُ لَهُ مَا أَثْبَتَهُ لِنَفْسِهِ،

Ndipo zitsutsidwe pa Iye zomwe Iyeyo  
Mwini Wake adazitsutsa (kuti si mbiri  
Zake).

وَيُنْفِي عَنْهُ مَا نَفَاهُ عَنْ نَفْسِهِ.

تَمْرِين

NTCHITO

**1. Kodi Tawhīd ili m’mitundu ingati?**

Mwana adziwe mitundu yonse itatu ya Tawhīd. Aphunzitsidwe kuti mitundu itatu imeneyi ikupezeka mu Qur’ān (Sūrah Maryam 19:65).

**2. Kodi Tawhīd Ar-Rubūbiyyah ndi chiyani?**

Mwana atambasule momveka bwino za Tawhīd imeneyi ndipo apereke zitsanzo zolondola.

**3. Kodi Tawhīd Al-Ulūhiyyah ikutanthauza chiyani?**

Mwana atambasule momveka bwino za Tawhīd imeneyi ndipo apereke zitsanzo za ‘ibādah. Mufotokoze kuti: kumukonda Allāh kwambiri kuposa aliyense; komanso kuzindikira kuti Allāh amaona zomwe timachita ngakhale tili tokha; komanso kupempha chitetezo mu chomwe tikuchiopa ndi gawo la Tawhīd imeneyi.

**4. Kodi msilamu akhulupirire chani pa Tawhīd Al-Asmā’ wa As-Sifāt?**

Mwana afotokoze kuti Tawhīd imeneyi ndi yomwe ena mu gulu la omwe amadzitcha kuti ndi asilamu adagalukira. Ena mwa iwo amamufananizira Allāh ndi zolengedwa Zake, ena amazikana mbiri Zake, ndipo ena amazisintha.

**5. Kodi Tawhīd yomwe Allāh adatilengera nayo ndi iti?**

Mwana adziwe kuti Tawhīd Al-‘Ibādah ndi yomwe adalengera anthu ndi ziwanda. Allāh asadatilenge kupatula kuti tidzamupembedze Iye Yekha basi.

# ضِدُّ التَّوْحِيدِ

## CHOTSUTSANA NDI TAWHĪD

Dziwa, chomwe chimatsutsana ndi Tawhīd ndi Shirk. **اعْلَمْ، أَنَّ ضِدَّ التَّوْحِيدِ الشِّرْكَ.**

Ndipo tikati Shirk: kumeneku ndiko kumupatsa Allāh bwenzi. **وَالِإِشْرَاكُ: هُوَ اتِّخَاذُ شَرِيكًا لِلَّهِ؛**

Kapena kutenga wopikisana ndi Allāh mu

**أَوْ اتِّخَاذُ نِدًّا لِلَّهِ فِي**

Mitundu itatu ija ya Tawhīd.

**ثَلَاثَةِ أَقْسَامٍ التَّوْحِيدِ.**

Ndipo Shirk imeneyi ilipo Mitundu iwiri:

**وَالشِّرْكَ نَوْعَانِ:**

Shirk yaikulu ndi Shirk yaing'ono.

**شِرْكَ أَكْبَرُ وَشِرْكَ أَصْغَرُ.**

Tsopano tikamakamba za Shirk Yaikulu;

**فَأَمَّا الشِّرْكَ الْأَكْبَرُ؛**

Ndipo Shirk ndi pamene kapolo watenga chinthu china posakhala Allāh...

**فَهُوَ اتِّخَاذُ الْعَبْدِ غَيْرِ اللَّهِ...**

Kukhala chopikisana ndi Iye (Allāh), chofanana komanso choyerekezedwa (ndi Allāh).

**نِدًّا بِهِ مُسَوِّيًا مُضَاهِي.**

Amapita kwa ichocho (chifanocho) mu nthawi yomwe vuto lamugwera munthuyo... **يَقْصِدُهُ عِنْدَ نَزْوِلِ الضَّرِّ...**

Kuti apezeko ubwino kapena achotsetse choipa (chamugweracho). **لِجَلْبِ خَيْرٍ أَوْ دَفْعِ شَرِّ.**

Kapena pa chilichonse chomwe fanolo silingathe kukwanitsa **أَوْ عِنْدَ أَيِّ غَرَضٍ لَا يَقْدِرُ عَلَيْهِ...**

Kupatulapo Mwini Wokutha kuchita zinthu (Yemwe ndi Allāh). **إِلَّا الْمَالِكُ الْمُقْتَدِرُ.**

Tsopano ikakhala Shirk yaing'ono: **وَأَمَّا الشِّرْكَ الْأَصْغَرُ:**

Ndi liwu lililonse kapena ntchito iliyonse **فَهُوَ كُلُّ قَوْلٍ أَوْ عَمَلٍ**

Yomwe imakhala njira yomugwetsera munthu mu Shirk yaikulu. **مَا يَكُونُ وَسِيلَةً إِلَى الشِّرْكِ الْأَكْبَرِ.**

تَمْرِين

NTCHITO

**1. Kodi chomwe chimatsutsana ndi Tawhīd ndi chiyani?**

Mwana adziwe kuti chimene chimatsutsana ndi Tawhīd ya munthu ndi Shirk.

**2. Kodi Shirk ndi chiyani?**

Mwana athe kufotokoza kuti Shirk ndi chiyani. Izi zimuthandiza kusiyanitsa pakati pa Tawhīd ndi Shirk zomwe zimawavuta kusiyanitsa ena mu gulu la anthu.

**3. Zingatheke kupeza thandizo la nzeru kwa munthu mnzathu?**

Mutha kupereka zitsanzo za ntchito zomwe palibe amene angakwaniritse kupatulapo Allāh Yekha basi. Izi zimuthandiza mwana kudziwa kuti sizili zoyenera kusaka thandizo kapena chitetezo kudzera mu zolengedwa za Allāh.

**4. Kodi Shirk ili mu mitundu ingati?**

Mwana athe kufotokoza mitundu iwiri ya Shirk.

**5. Kodi pakati pa munthu ndi Allāh, amene angathetse mavuto athu ndi ndani?**

Adziwe mwana kuti anthu sangachotse mavuto a anthu anzawo. Ndi Allāh Yekha amene ali ndi kuthekera kobweretsa vuto ndi kulichotsanso.

# أَمْثَلَةُ الشِّرْكَ

## ZITSANZO ZA SHIRK

Kuchokera mu zitsanzo za Shirk  
Yaikulu, ndi monga:

مِنْ أَمْثَلَةِ الشِّرْكِ الْأَكْبَرِ مَا يَأْتِي:

Kupanga Du'ā kwa wina posakhala kwa Allāh.

دُعَاءٌ غَيْرِ اللَّهِ.

Kupempha thandizo kwa wina posakhala kwa Allāh.

وَالِاسْتِغَاثَةُ بِغَيْرِ اللَّهِ.

Kupereka uzindikira wa zobisika kwa  
wina posakhala Allāh.

وَنِسْبَةُ عِلْمِ الْغَيْبِ إِلَى غَيْرِ اللَّهِ.

Ndipo kuchokera mu zitsanzo za  
Shirk Yaing'ono ndi monga:

وَمِنْ أَمْثَلَةِ الشِّرْكِ الْأَصْغَرِ مَا يَأْتِي:

Kulumbira posakhala mdzina la Allāh.

الْحَلْفُ بِغَيْرِ اللَّهِ،

Kuchita ntchito modzionetsera

وَالرِّيَا،

Komanso zithumwa (zomwe zimakolekedwa thupi, pa khoma  
kapena malo ena alionsewo).

وَالْتَّمَائِمِ،

Komanso kukhulupirira mu tsoka ndi mwayi kudzera mu zolengedwa.

وَالتَّطْيِيرِ.

تَمْرِين

NTCHITO

**1. Kodi zitsanzo zina ziti zimene mungapereke pa Shirk Yaikulu?**

Mwana ayesere kupereka zitsanzo zina ngati akuzidziwa. Koma ngati sakuzidziwa, mumupatse zina zochuluka kuposera zomwe tatchulazo monga: kumumvera munthu mu zomwe Allāh adaletsa; kunena kuti makolo ndi mulungu wachiwiri; kuchita ntchito za ‘ibādah pofuna kupeza za dziko lapansi; ndi zina zotero.

**2. Ndi zitsanzo zina ziti zimene mungapereke pa Shirk Yaing’ono?**

Mupatseninso zitsanzo zina pa gawo limeneli.

**3. Kodi kumupempha Yesu kapena Muhammad ndi kololedwa?**

Mwana aphunzitsidwe momveka bwino kuti omwe amapempha mtumiki wina aliyenseyo amachita Shirk Yaikulu.

**4. Kodi msilamu akhulupirire chani pa nkhani ya Shirk Yaikulu?**

Mwana athe kufotokoza kuti Shirk Yaikulu ndi chinthu chimene chikamukhazike munthu ku Moto mpaka kalekale.

**5. Kodi nanga Shirk Yaing’ono ili ndi zotsatira zotani pa msilamu?**

Mwana azindikire kuti Shirk Yaing’ono imapungula Tawhīd ya munthu, komanso imaongonga ntchito yokhayo imene yakhudzana ndi Shirk imeneyi, ndipo ndi njira yomugwetsera munthu ku Chilango chowawa cha Moto chomwe atakachilawe kwa nthawi yaitali.